PHUNZIRO LA 59

1.Kodi chifukwa chiyani Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo anakwiya ndi ophunzira a Yesu?
-Chifukwa chakuti ophunzira a Yesu sankasunga miyambo ya akuluakulu.

2. Kodi miyambo ya akuluakulu inali chiyani?
-Inali miyambo imene Afarisi anakhazikitsa imene ankati kuti anthu ayenera kumayitsatira kuti akalandiridwe ndi Mulungu.

3. Kodi Mulungu amaŵalandila anthu chifukwa cha miyambo ya makolo imene amayisunga?
-Ayi.

4. Kodi Mneneri Yesaya analankhula chiyani za anthu ameneŵa?
-Mneneri Yesaya analankhula kuti anthu ameneŵa amangolankhula ndi milomo yawo yokha kuti akumukhulupilira Mulungu, koma mitima yawo ili kotalikana ndi Mulungu.

5. Chifukwa chiyani Mulungu sankakulandira kupembedza kwa Afarisi?
-Chifukwa chakuti kupembedza kwawo kunali kwa thupi lawo lokha osakhala kochokera m'mitima yawo.

6. Kodi Mulungu amafuna kuti anthu adziwonjezera miyambo yawo ku Buku Lache, Bayibulo?
-Ayi.

-Tisadzayelekeze kuwonjezera kapena kuchotsa china

chilichonse chimene Mulungu walankhula M'bayibulo.

7. Kodi chifukwa chiyani anthu sangadetsedwe ndi kusasamba m'manja kapena chakudya chosatsuka?
-Chifukwa chakuti zimenezi sizikhuza mtima.

8. Kodi Mulungu angatilandire chifukwa cha zinthu zimene ife timadya?
-Ayi.

9. Kodi Mulungu angatilandire chifukwa cha zinthu zimene ife sitimadya?
-Ayi.

10. Kodi Yesu analankhula kuti ndi chiyani chimene chingamupangitse munthu kukhala odetsedwa?
-Yesu analankhula kuti chimene chili mkati mwa munthu ndi chimene chingamupangitse munthuyo kukhala odetsedwa.

11. Kodi zoyipa zimene zili mkati mwa mtima wa munthu aliyense ndi zotani?
-Maganizo oyipa, kugwilira, kuba, kupha, chigololo, umbombo, msanje, bodza, mwano, miseche, kudzikweza ndi kupusa.

12. Kodi mu fanizolo, ndi ndani amene anapita ku Nyumba ya Mulungu kukapemphera?
-M'modzi anali Mfarisi ndipo wina anali okhometsa msonkho.

13. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamukana Mfarisi uja?



Wawo.

-Kodi Mulungu Atate ankatanthawuza chiyani?
-Mulungu Atate ankatanthawuza kuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi weniweni, amene ankamukonda kwambiri.

-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi, ophunzira a Yesu anayenera kumumvera Iye.

-Kodi lero, Mulungu amalankhula ndi ife kuchokera kumwamba?
-Ayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti zonse zimene Mulungu amafuna kutiwuza ife zalembedwa m'Buku Lache, Bayibulo.

-Mulungu akufuna kuti ife timumvere Yesu pamodzi ndi Mawu ache amene alembedwa M'buku la Mulungu, Bayibulo.

-Mulungu Atate anaŵatumiza iwo kuchokera kum-
wamba kudzalankhulana ndi Yesu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu Atate anafuna kuti Eli-
ya ndi Mose adzalankhulane ndi Yesu?
-Mulungu Atate ankafuna kuti Mose ndi Eliya amulim-
bikitse Yesu pa imfa imene ankadza kwa Iye.

-Kodi kenako chinachitika ndi chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 9:5-8

5-Kenako Petulo analankhula kwa Yesu mokwe-
za mawu, "Mphunzitsi, kwatikomera kuti ife tili pompa-
no, ndipo timange misasa itatu, limodzi la Inu, limodzi
la Mose, limodzi la Eliya."
6-Onse atatu, anali ndi mantha mwakuti
sankadziŵa zimene ankalankhula.
7-Kenako linawoneka thambo ndikuŵaphimba
iwo, ndipo mawu anamveka kuchokera mu thambomo
akuti, "Uyu ndiye Mwana wanga okondedwa, mverani
Iye"
8-Mwadzidzidzi, pamene ankati ayan-
g'aneyang'ane, palibe amene anamuwona koma Yesu
yekha.

-Kodi mawu amene anachokera mu thambo lija anali a
Ndani?
-Mulungu Atate.

-Kodi Mulungu Atate analankhula chiyani kwa
ophunzira a Yesu?
-Mulungu Atate analankhula kuti Yesu anali Mwana



-Chifukwa chakuti iye sankakhulupilira kuti anali ndi
mtima oyipa
-Chifukwa chakuti iye sankakhulupilira kuti ana-
muchimwira Mulungu.

14. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamulandira iye?
-Chifukwa chakuti iye anadziŵa kuti anali ndi mtima
oyipa.
-Chifukwa chakuti iye anadziŵa kuti wamuchimwira
Mulungu.
-Chifukwa chakuti iye anamupempha Mulungu kuti
amupulumutse.

-Tsiku lina, Yesu anaŵafunsa funso ophunzira ache.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 8:27-28

27-Yesu pamodzi ndi ophunzira ache anapita ku
midzi yozungulira ku Kayisariya Filipi. Ali mu njira,
Yesu anaŵafunsa ophunzira ache kuti, "Kodi anthu
akuti Ine ndani?"
28-Ophunzira achewo anayankha kuti, "Ena
akuti Inu ndi Yohane M'batizi, ena akuti Inu ndi Eliya;
komabe ena akuti Inu ndi m'modzi mwa aneneri."

-Kodi ndi funso lotani limene Yesu anaŵafunsa
ophunzira ache?
-Yesu anafunsa kuti, "Kodi anthu akuti Ine ndani?"

-Kodi ophunzira a Yesu anayankha kuti chiyani?
-Anthu ena ankaganiza kuti Yesu anali Yohane
M'batizi
-Anthu ena ankaganiza kuti Yesu anali Eliya.

-Anthu ena ankaganiza kuti Yesu anali m'modzi mwa aneneri.

-Kodi chifukwa chiyani anthu ena ankaganiza kuti Yesu anali Yohane M'batizi?
-Chifukwa chakuti Mfumu Herodi anapha Yohane M'batizi, anthu ena ankaganiza kuti Yesu ndi Yohane M'batizi amene wadzukanso ku imfa.

-Kodi Yesu anali Yohane M'batizi?
-Ayi.

-Nanga chifukwanso chiyani anthu ena ankaganiza kuti Yesu ndi Eliya?
-Kodi Eliya anali ndani?
-Eliya anali mneneri amene sanafe pa dziko la pansi koma anatengedwa ndi Mulungu mwini, ndikupita naye kumwamba.

-Kodi Yesu anali Eliya?
-Ayi.

-Nanga chifukwanso chiyani anthu ena ankaganiza kuti Yesu anali m'modzi mwa aneneri amene wadzuka kuchokera ku imfa?
-Chifukwa chakuti aneneri ankalankhula za Mulungu ndipo ankaŵayitanira anthu kolapa machimo.

-Kodi Yesu anali m'modzi mwa aneneri amene anadzuka kuchokera ku imfa?
-Ayi.

-Kodi kenako Yesu anaŵafunsa funso lotani ophunzira



-Koma mkati, Yesu anali Mulungu.

-Yesu anali Mulungu weniweni ndiponso munthu weniweni.

-Mwadzidzidzi, panawoneka anthu aŵiri pafupi ndi Yesu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 9:4

4-Kenako ophunzira atatu aja anamuwona Eliya ndi Mose akulankhulana ndi Yesu.

-Kodi Eliya anali ndani?
-Eliya anali mneneri wa Mulungu amene anabwera pa dziko la pansi Yesu asanabadwe pa dziko la pansi

-Mu zaka zambiri zapitazo, Eliya asanafe, Mulungu anamutenga iye ndikupita naye kumwamba.

-Kodi Mose anali ndani?
-Mose anali munthu amene anaŵatsogolera a Isirayeli poturuka mu dziko la Iguputo.

-Mu zaka zambiri zapitazo, Mose anafa, ndipo Mulungu anawutenga mzimu wache ndikupita nawo kumwamba.
-Chifukwa chakuti Eliya ndi Mose ankakhulupilira mwa Mulungu, akukhalabe ndi Mulungu kumwamba mpaka lero.

-Kodi Eliya ndi Mose anabweranso bwanji pa dziko la pansi pano?

-Zitatha izi, Yesu anatenga Peturo, Yakobo ndi Yohane, nakwera nawo phiri lalitari.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 9:2-3

2-Patatha masiku asano ndi limodzi, Yesu anatengera padera Peturo, Yakobo, ndi Yohane , nakwera nawo phiri lalitari. Kumeneko, kawonekedwe ka Yesu kanasandulika pa maso pawo.
3-Zovala zache zinakhala zonyezimira, zoyera mbee, mwakuti palibe amene angathe kuchapa zovala pa dziko la pansi ndi kuziyeretsa chomcho.

-Kodi chinachitika kwa Yesu ndi chiyani pa phiri paja?
-Yesu anasanduka pamaso pa Peturo, Yohane ndi Yakobo.

-Kodi zikutanthawuza kuti chiyani ndi kusanduka kwa Yesu?
-Zikutanthawuza kuti Mulungu amene anali mkati mwa Yesu anawonekera kunja.

-Ngakhale kuti Yesu anali ndi thupi la umuthu panja, analinso Mulungu mkati mwache.

-Kodi mukulikumbukira hema limene Mose anamanga pamodzi ndi a Isilayeli?
-Panja pa hemalo panali zikopa za nyama, koma mkati munali ulemelero wa Mulungu.

-Anthu akamuwona Yesu, ankangowona munthu kunja.



ache?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 8:29

29-Kenako Yesu anaŵafunsanso kuti, “Nanga inu mukuti Ine ndi ndani?” Petulo anayankha kuti, “Inu ndi Kilisitu.”

-Kodi kenako Yesu anaŵafunsanso chiyani ophunzira ache?
-Yesu anaŵafunsa kuti, “Kodi nanga inu mukuti Ine ndani?”

-Kodi Peturo anayankha kuti chiyani?
-Peturo anayankha kuti, “Inu ndi Kilisitu.”

-Petulo anadziŵa kuti Yesu anali Kilsitu amene Mulungu anamulonjeza kwa Adamu ndi Hava m’munda wa Edeni.

-Petulo anadziŵa kuti Yesu anali Kilsitu amene Mulungu anamulonjeza kwa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo.

-Petulo anadziŵa kuti Yesu anali Kilsitu, Mulungu Mpulumutsi.

-Ngakhale kuti Yesu anaŵawuza Ayuda nthaŵi zambiri, ambiri mwa iwo sankakhulupilirabe kuti Iye anali Mulungu Mpulumutsi.

-Kodi ngati ife sitikukhulupilira kuti Yesu ndi Mulungu Mpulumutsi, tingapulumutsidwe?
-Ayi.

-Kodi pa tsiku lotsatira lachelo Yesu analankhula chiyani kwa ophunzira ache?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 8:30

30-Yesu anaŵachenjeza kuti asamuwuze munthu wina aliyense za Iye.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anaŵachenjeza kuti asamuwuze aliyense za Iye?
-Yesu sankafuna kuti anthu akhulupilire chifukwa cha wina aliyense.

-Yesu ankafuna kuti anthu akhulupilire kuchokera m'mitima mwawo.

-Ngati tikukhulupilira mwa Yesu, chikhulupiliro chimenechi chiyenera kuchokera m'mitima mwathu.

-Sitingathe kukhulupilira mwa Yesu kuchokera kwa munthu wina aliyense.

-Zitatha izi, Yesu anayamba kuŵaphunzitsa ophunzira ache za zimene zinkadza.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 8:31

31-Kenako [Yesu] anayamba kuŵaphunzitsa ophunzira ache kuti, "Mwana wa munthu akuyenera kuvutitsidwa kwambiri ndiponso kukanidwa ndi akuluakulu a Ayda, akuluakulu amsembe, ndi aphunzitsi a malamulo. Ndipo adzaphedwa, koma adzawukanso



patapita masiku atatu."

-Kodi Yesu anaŵaphunzitsa chiyani ophunzira ache za zimene zinkadza?
-Yesu anaŵaphunzitsa kuti akuluakulu a anthu adzamupha Iye, koma adzawukanso kuchokera kwa akufa patatha masiku atatu.

-Kodi Yesu ankadziŵa bwanji za zimene zinkadza?
-Yesu ndi Mulungu ndipo amadziŵa zinthu zonse.
-Palibe chimene sangachidziŵe Yesu.

-Yesu anadziŵa kuti akuluakulu a anthu adzamupha Iye.

-Yesu anadziŵa kuti Iye ayenera kufa.

-Komanso Yesu anadziŵa kuti adzawukanso kuchokera kwa akufa pakadzatha masiku atatu.

-Kodi mukukumbukira kuti Yona anakhala usana ndi usiku ungati m'mimba mwa msomba yayikuru ija?
-Usana utatu ndi usiku utatu.

-Ngati m'mene Yona anakhalira m'mimba mwa msomba yayikuru ija usana utatu ndi usiku utatu, chomchonso Yesu adzakhala m'mimba mwa mthaka usana utatu ndi usiku utatu.

-Ngati m'mene Yona anakhaliranso ndi moyo patatha usana utatu ndi usiku utatu, Mulungu adzamudzutsanso Yesu kuchokera kwa akufa patatha usana utatu ndi usiku utatu.